

LIU LA NAMIKANGO

Namikango Mission

Volume 18(2), June 2018



Kupitiriza mu Buku la Luka 15

Moni kuchokera ku Mishoni ya Namikango! Ndife osangalala kukupatsani Liu lina ndi kupitiliza kukambirana kwathu kumene kunayamba m'mbuyomu. Kumbukirani nane pamodzi nkhani imene tinakambirana mu Liu lathu loyamba Tinakambirana Luka 15 monga nyumba imene tikhoza kukhalamo ndi kumaonera dziko lapansi kudzera m'menemo. Tinafotokoza kuti mafanizo onse atatu amene akupezeka m'mutu 15 wa Luka amatiuza chimene Mulungu ali, komanso m'mene Mulungu amalankhulira ndi anthu. Tikudziwa kuti Yesu akamanena mafanizo, iye akutipatsa ife nkhani yokhudza chimene Mulungu ali komanso chimene Mulunguyo amaganiza zokhudza chilengedwe chake. Yesu akutipatsa nkhani zitatu zosiyana zokhudza Mulungu, ndipo iliyonse mwa nkhani zimenezi zikutipatsa ife uthenga wabwino!

Kumbukirani kuti fanizo loyamba limene likupezeka mu Luka 15 likufotokoza za m'busa amene akuzindikira kuti nkhoa yake yasokera. M'busa wabwinoyu akupita m'chipululu ndicholinga chakuti akapeze nkhoa yosokerayi.

Iye akuyang'anayang'ana, nthawi zambiri m'malo oopsa ndicholinga chakuti abwezeretse nkhoa yakeyo kukhola. M'busa uyu ndi wabwino, chifukwa amasamala kwambiri nkhoa zake. Palibe nkhoa imene imasokera mopanda chiyembekezo kapena kutalikiratu ku chikondi cha m'busa wabwino.

Mu m'njira yomweyi, Mulungu amatisakanso ife tikasokera. Iye samatisiya mchipululu kuti tife, kapena kutiyang'ana ndi cholinga chakuti atilange chifukwa choti tinasokera. M'malo mwake, Mulungu amatiyang'ana chifukwa iye amatikonda ndipo amafuna kutiteteza ku zoopsa za mchipululu.

Mulungu akatipeza, samatilanga, koma amatinyamula kupita nafe kukhola kumene tingatetezedwe.

Pamene fanizo limeneli likutipatsira uthenga wabwino, tikudziwa kuti ndi fanizo lokhalo mwa atatu limene Yesu akutiuzwa mu Luka 15. Mu Liu lino, tikufuna kuchoka ku fanizo loyamba lokhudza m'busa wabwino amene akuyang'ana nkhoa yake ndi kupita ku fanizo lachiwiri la Yesu, la mzimayi wabwino amene akuyang'ana ndalama yake yotaika. Sungani mfundo za mu fanizo la m'busa wabwino m'mutu mwanu pamene mukuona fanizo lachiwiriri, ndipo muone ngati pali kulumikizana pakati pa nkhani ziwirizi. Dzifunse nokha zam'mene m'busa wabwino ndi mzimayi wabwino ali ofananirana. Mudzifunse za chimene Yesu akufuna kunena ndi fanizo lachiwiriri. Kodi fanizo lachiwiriri lokhudza mzimayi wabwino likutipatsanso uthenga wabwino?

Monga m'mene tinanenera m'mbuyomu, pamene mukuwerenga ndi kulingalira pa fanizo lachiwiriri, yesetsani kuti mudzidzipezanso inuyo mu nkhanayi. Taganizirani za m'mene mungachitire ngati mutataya ndalama yanu, ndi m'mene ndalamayo ingamvere kutaika ndi kupezeka. Pomaliza, dzifunse nokha pazimene mungaphunzire zokhudza Mulungu mu fanizo limeneli. Pezani zinthu zatsopano zokhudza inu eni komanso Mulungu pamene mukulingalira pa fanizo lachiwiriri.

-Eric Gephart

Fanizo la Ndalama Yotaika

Kumbukirani kuti kuchokera mu nkhani yathu ya m’mbuyomu, mafanizo atatu amenewa (la nkhosa, Ndalama ndi ana awiri) ndi ziphunzitso za Yesu ku magulu awiri a anthu: “anthu ochimwa” ndi “a Afarisi” (15:1-3). Kumbukirani kuti m’busa anapita kukayang’ana nkhosa, anaipeza nkhosa ija, ndipo anasangalala ndi anzake chifukwa inapezeka. Kenako, tili ndi fanizo lachiwiri, fanizo la ndalama yotaika. Pamenepa tili ndi fanizo lofanana koma laling’ono. M’ malo mwa malo aakulu, tili ndi chipinda chimodzi. M’ malo mwa nkhosa 100, tili ndi ndalama za makoini khumi. Komabe imodzi yokha ikusowa (monganso nkhosa imodzi) inasowa.

Ngakhale kuti abusa mu nthawi ya Yesu, komanso masiku anthu ano, akhoza kukhala amuna kapena akazi. Fanizoli likufotokoza za mzimayi wabwino. Iye, monganso m’busa wabwino, ndi okhudzidwa ndi ndalama yotaikayi. Mwina ali ndi mantha kuti mwamuna wake akwiya naye kapena mwinanso ndalamayo ndi yambiri yoti akalipilire ku sukulu kwa mwana. Mulimonse, iye akuona kufunikira kwa ndalamayi ndipo akusesa mnyumba, kugwiragwira, kugwada kuti apeze ndalama yotaikayi; ntchito yaikulu kufuna ndalama imodzi yokha. Mofanana ndi nyumba zakale zambiri zimene zinamangidwa ku Malawi kuno, nyumba imeneyi mwina inalibe mazenera choncho munali mdima. Mwinanso pansi pake panali popanga ndi njerwa kapena miyala, ndiye ndalamayi ikhoza kukhala kuti inagwera pakati pa ming’alu kupangitsa kuti kukhale kovuta kuiona.

Kusiyana ndi nkhosa ija, ndalamayi siinapite kutali. Siinayesere kupita kutali kusochera. Siinathawe kumusiya mwini wakeyo. Inataidwa ndi mwini wakeyo; inaikidwa malo osadziwika kapena kuiwalidwa mpaka kufikira mwini wakeyo anazindikira ndi kuyamba kuifunafuna. Koma kenako, mwini wakeyo, m’zimayi wabwino waipeza ndalama ija! Akuitana anzake, “Bwerani musangalale nane, Ndaipeza ndalama yotaika ija!” Umu ndi m’mene zimakhallira pamene Mulungu amasaka wina aliyense wa ife (ndalama zake zotaika) ndi

Luka 15:8-10

Kapena mkazi wanji ali nazo ndalama zasiliva khumi, ngati itayika imodzi, sayatsa nyali, nasesa m’nyumba yake, nafunafuna chisamalire kufikira akaipeza? Ndipo m’mene aipeza amema abwenzi aka ndi anansa ake, nanena, Kondwerani ndi ine, chifukwa ndinapez ndalama ndidatayayo. Chomwecho, ndinena kwa inu, kuli chimwemwe pamaso pa angelo a Mulungu chifukwa cha month wochimwa mmodzi amene atembenuka mtima.

kutipeza! Kumwamba kumakhala phwando chifukwa cha chikondi chimene Mulungu alinacho pa ndalama zake.

Nkhani imeneyi ndi fanizo. Cholinga chake sikutipatsa ife uthenga watsopano koma kufunsa owerenga kuti akhale mu nkhaniyi. Kodi inuyo ndi uti mu nkhaniyi lero? Kodi mwataika ndipo mukufunika mutapezeka? Kodi mukufunafuna ndi kupemphelera munthu wina kuti apezeke? Kapena mwina ndinu opezeka – monga ndalama zina 9 zija – ndipo mwakhala mukudikira, osadziwa kuti muchite chiyani? Ndime imeneyi ikukuitanani kuti muchitepo kanthu lero. Fanizo limeneli likufunsa ngati muli ndi mtima ofanana ndi mzimayi wabwinoyu, mtima wa Mulungu. Kodi muli ngati mzimayi wabwino amene mukuchita chilichonse chotheke kuti mupeze ndalama imodzi, munthu m’modzi? Kodi m u m a s a n g a l a l a m u n t h u m ’ m o d z i akapululumutsidwa? Kodi mumakhumba mutaona anthu akubwezeretsedwanso kwa Mulungu? Kapena simusamala za m’bale kapena mlongo wanu amene ali otaika? Kodi nthawi yanu imangothera kuonera mpira, kumvera wailesi kapena kuchita malonda anu, kapenanso mumatenga gawo kufuna amene dera lanu limanena kuti ndi “ndalama zotaika”? Yesu anatiitana kuti tidzikachita zimene iye ankachita (Luka 4:14-19; Luka 19:10), kufunafuna ndi

kupulumutsa chotaika, kuchiza miyoyo ya opweteka ndi ochimwa, kuti adziwe kuti Mulungu amawakonda kwambiri mpaka anawafera.

Fanizo limeneli likutionetsa kuti sitikuyenera kungokhala pamene tapezeka. Tayanjanitsidwa (tapezeka) kuti tikakhale akazembe achiyanjanitso (2 Akorinto 5:18-21). Tikuyenera kuonetsa anthu ena m'mene Mulungu amawakondera komanso m'mene Mulunguyo akufunira kuti ayanjanitsidwe naye. Kodi tikusiiranjiki kufunafuna ndalama zotaika pamene tikudziwa kuti Mulungu amafunafuna izo nthawi zonse? Kodi tikukhaliranjiki okhutitsidwa kungowasiya anthu kukhala otaika pamene Mulungu sakukhutitsidwa kuti akhalebe otaika? Mulungu sadzasiya kukufunani mpaka mutapezeka. Kodi inu mudzasiya kufunafuna m'bale kapena mlongo wanu mpaka atapezeka? Tiyeni tikhale ngati mzimayi wabwinoyu lero – kufunafuna ndalama zotaika m'madera athu mpaka zitapezeka, kenako mkusangalala kuti apezeka.

Mafunso olingalira ndi kukambirana:

1. Kodi inu ndinu ndani lero? Mzimayi wabwino kapena ndalama yotaika?
2. Kodi kufanana kwa pakati pa nkhusa ndi ndalama yotaika mu nkhanizi ndi chiyani?
3. Kodi kufanana kwa pakati pa m'busa wabwino ndi mzimayi wabwino ndi ziti?
4. Kodi kuona Mulungu monga mzimayi wabwino kukutithandiza kumvetsetsa chikhalidwe cha Mulungu bwanji? Werengani ndime izi kuti mulingalire kwambiri: Yesaya 66:10-13; Deuteronomo 32:18; Yesaya 46:3-4; Luka 13:34.

5. Kodi fanizo la ndalama yotaika likuonjezera kumvetsetsa kwa fanizo la nkhusa yotaika bwanji?

6. Ngati Mulungu ali ngati mzimayi wabwino, kodi zimenezi zingaonjezere kumvetsetsa kwathu bwanji pa udindo wa mpingo pakufunafuna otaika?

7. Ngati mwakhala gawo lophwanya ubale ndi wina wake mu mpingo kapena kunjwa kwa mpingo, tsopano panopa mupanga bwanji monga mzimayi wabwino pakufunafuna ndi kubwezeretsa ubale umenewo?

-Ryan Hayes

Zowerenga Zina

Tsopano takhala ndi nthawi kulingalira za fanizo lachiwiri la Yesu lokhudza mzimayi wabwino ndi ndalama yake yotaika, tikhoza kulumikiza fanizo limeneli ndi nkhanzi yonse ya M'Baibulo. Mu gawo lino, ndikufuna ndikupatseni ndime zoti muwerenge komanso kulingalira. Pamene mukuwerenga ndime zimenezi, dzifuneni nokha mafunso pazimene mukuwerenga zokhudza Mulungu komanso anthu mu ndime iliyonse. Ndiponso mudzifunse m'mene ndime zimenezi zingamvetsetsedwere kudzera mu fanizo la Yesu lokhudza mzimayi wabwino ndi ndalama yake yotaika. Kodi mungalumikize ndime zimenezi kuti mupeze kumvetsetsa kwenikweni komanso chithunzithunzi cha Mulungu komanso chikondi chake pa ife?

Mu Masalimo 23 tikuona Wolemba Masalimo akulemekeza ndi kufotokoza Mulungu mu njira zosiyanasiyana. Mu ndime 1 mpaka 3 wolemba Masalimo akumufotokoza Mulungu monga m'busa wabwino amene amapereka zosowa za nkhusa zake. Mulungu amadyetsa nkhusa zake, amazimwetsa madzi, ndi kuziteteza. Komano tikuona chithunzi chikusintha kuchoka

ku m’busa wabwino kupita kwa mzimayi wabwino. Mu ndime 5 wolemba Salimoli akuti Mulungu amamukonzera gome kuti adyerepo, amamudzodza mafuta ndiponso amamupatsa nyumba yoti akhalemo. Zochitika zonsezi mwachikhalidwe zimachitidwa ndi mkazi wa mnyumbamo. Monga m’mene zilili ku Malawi kuno, chonchonso mu nthawi ya Baibulo, ndi mkazi amene amakonza pa gome ndi chakudya, amene amalandira alendo kunyumba, komanso kusamala m’nyumba kuti ikhale yabwino ndi yosamalika. Chifukwa cha chimenechi, mu Salimo lodziwikali, tikuona Mulungu akufotokozeredwa monga m’busa wabwino komanso mzimayi wabwino, monga Yesu akuchitira mu Luka 15! M’musimu muli Masalimo ena oti inuyo muwerenge ndi kulingalira:

- Masalimo 17:8-9
- Masalimo 36:7-9
- Masalimo 57:1
- Masalimo 61:4
- Masalimo 123:2
- Masalimo 131:2
- Yobu 38:28-29

Mverani Ine, banja la Yakobo, ndi otsala öonse a banja la Israele, amene ndakunyamulani kuyambira m’bimba, ndi kukusenzani chibadwire; ngakhale mpaka mudzakalamba Ine ndine, ndipo ngakhale paka tsitsi laimvi, Ine ndidzakusenzani inu; ndalenga, ndipo ndidzanyamula; inde, ndizasenza, ndipo ndidzapulumutsa. -Yesaya 46:3-4

Mu Numeri 11 a Israyeli akungoyendayenda kuzungulira m’chipululu. Patatha nthawi pang’ono, iwo anakwiya chifukwa chakuti anakhala nthawi yaitali mchipululu muja, ndipo anayamba kudandaula kwa Mose komanso Mulungu. Mose anakwiya kwambiri ndipo anamufunsa Mulungu kuti alowerere mu nyengo yawo. Mu ndime 12, Mose akumufunsa Mulungu ngati a Israyeli anawabala ndi Moseyo kapena Mulunguyo. Mose akuvomereza kuti anthuwa akufunikira munthu wa mayi kuti awayang’anire, koma Mose sangakwaniritse ntchito imeneyo. Choncho, Mose akuuza Mulungu kuti awasamalire anthuwa monga mayi asamalira ana ake. Werengani ndi kulingalira ndime zimenezi kuchokera mu Chipangano Chakale. Pamene mukuwerenga malemba, mudzidzifunsa nokha kuti kodi nkhani zimenezi zimatiuza chiyani zokhudza Mulungu komanso ndi m’mene

amakhallira ndi anthu ake. Kodi nanga alembi a Baibulo amamufotokoza bwanji Mulungu?

- Numeri 11:12
- Deuteronomo 32:11-12
- Deuteronomo 32:18

Mu Yesaya 49:15 Mulungu akuti, “Kodi mkazi angaiwale mwana wake wa pabere, kuti iye sangachitire chifundo mwana wobala iye. Inde awa angaiwale, koma Ine sindingaiwale iwe.” Mu ndime imeneyi Mulungu akuti mayi wabwino sangaiwale ana ake koma adzaonetsera chifundo kwa anawo. Kenako Mulungu akuti iye ali ngati amayi abwinowa, iye sadzatiwala ife, ana ake. Mulungu ali ngati mzimayi wabwino uja, iye

amakumbukira anthu ake, iye amawateteza ndi kuwasamalira. Iyi ndi nkhani yabwino ndithu kwa ife! Lingalirani ndime zimenezi kuchokera kwa aneneri mu Chipangano Chakale. Dzifunsemi nokha m’mene Yesaya ndi Hoseya akufotokozerana Mulungu komanso chimene zimenezi zikuti uza ife pa zam’mene Mulungu amatisamalirira ife.

- Yesaya 42:14
- Yesaya 46:3-4
- Yesaya 66:10-13
- Hoseya 11:34
- Hoseya 13:8

Werengani ndime zotsatirazi kuchokera mu Chipangano Chatsopano. Pamene mukuwerenga ndime iliyonse, khalani ndi nthawi yoyankha mafunso awiri: Kodi ndime imeneyi imanena chiyani za anthu? Kodi nanga ndime imeneyi ikufotokoza chiyani za Mulungu komanso m’mene iye amalumikizirana ndi anthu?

- Mateyu 23:37
- Luka 13:34
- 1 Petro 1:22-23
- 1 Yohane 3:9-10

-Eric Gephart